

MLANDU



Atate athu Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha mwayi umene ife tiri nawo wodzasonkhana pansi pa denga ili masana ano, kachiwiri, kuti tidzamvetsere Mawu a Mulungu, ndi kudzawona ulemelero wa Ambuye Yesu Khristu. Ife tiri pansi pa ziyembekezo zazikulu, Atate. Ndipo tikupemphera kuti Inu mutilandire ife masana ano, ndi kulemekeza kuyesetsa kwathu kumene ife tayika kuti tibwere kudzakupembedzani Inu. Mudalitse moyo uliwonse umene uli pano. Tikuzindikira kuti zinthu zabwino ndi zomwe zimakhala zovuta kuzipeza. Kotero ife tikupemphera, kuti chifukwa cha nsembe yawo, pasakhale wina aliyense amene ati asiyidwe koma amene ati achiritsidwe masana ano. Pulumutsani otayika ndipo mupeze ulemelero kwa Inumwini. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Mukhoza kukhala pansi.

² Denga lathu la malatali limapangitsa kuti zikhale zovuta kuti mudzimva. Ife sititenga nthawi yayitali koma yapang'ono chabe, kuti tiyankhule ndi inu. Ndiye kenako ife tipitirirabe ndi mzere wa pemphero, chifukwa ndicho chimene ife tinachikonzera masana ano, chinali kuti tidzapempherere odwala.

³ Ndipo tsopano ine ndikufuna kunena ichi. Ine sindikudziwa kuti ndi liti pamene ndinasangalalapo kukhala ndi gulu la anthu monga momwe ndiliri ndi gulu ili pano. Inu mwakhala abwino kwenikweni. Ine ndimamuuza M'bale Johnson, kanthawi kapitako, kuti ine sindikudziwa ndi liti ndinayamba ndasangalalapo ndi msonkhano mwabwinoko kuposa uwu. Mzimu wopambana chotero pakati pa anthu inu, ndi kukhulupirira, chikhulupiriro. Ndikufuna kukhala kuno pafupifupi kwa mwezi, kuti tikhoze kudziwana kwenikweni wina ndi mzake. Kawirikawiri, nthawi imene mmayambira kudziwana, ndiye imakhala nthawi imene mmayenera kuti muziti “bayibayi” ndi kumapita kwinakwake.

⁴ Ine sindikudziwa amene wapolisi wamng'ono uyu ali kunja kuno, wayima kunja uko mu mvula yonseyo, mutu wopanda chipewa, akuyesetsa kulondolera magalimoto amenewo. Ngati winawake akumudziwa iye, mukandithokozere ine mwapadera, inu mukatero? Ine ndikukuuzani, iye wachita ntchito yabwino kwenikweni.

⁵ Ine ndikufuna kumuthokoza mwamuna amene anabwera kuno ndi kudzakonza malo awa, ndi kuwakonzekeretsa iwo kwa izi, kuti msonkhano uwu ukhoze kudzakhala pano lero. Ine ndikukuuzani inu, anthu ozungulira amayenera kupereka

ulemu wawukulu kwa amuna olimba mtima amenewo, amene angachite zimenezo. Ine ndiri ndi ulemu wawukulu kwa inu, chifukwa cha anthu amene angatuluke pa tsiku ngati ili. Anthu ambiri akanangokhala kwawo. Ine—ine ndikuyamikira kulimba mtima kwanu. Ndipo inu mutayima pano pakati pa zovuta zonsezi, mutakhala pansi pa denga ili, kumavutikira kuti mumvetsere zimene zikuchitika, komabe wotsimikiza kukhalabe mulimonse. Uko—uko ndiko kulimba mtimako. Ine—ine ndimazikonda zimenezo. Ine nthawi zonse ndimaganizira za nyimbo ijayi:

Kodi ndinyamulidwe kupita kwathu
Kumwamba
Pa bedi lamaluwa la wofuwofu,
Pamene ena anamenyera kuti apeze mphotoyo,
Ndipo anayandama kudutsa mu nyanja
zamazazi? (Eya, zovuta!)

⁶ Ine ndinalalikira, nthawi yina osati kale, mu South Africa, kumene inkavumba mwamphamvu kwambiri mu nthawi ya mvula yamkuntho, mpaka akazi, atakhala paliponse ndipo tsitsi lawo likugwera pansi, anali atakhala pamenepo tsiku lonse mu mvula imeneyo. Ine sindinayambe ndawonapo msonkhano wamachiritso woterowo mmoyo mwanga!

⁷ Ku Mexico, osati kale kwambiri, ine ndikukumbukira nditayima kumusi uko ndikulalikira, pamene inali ikuvumba monga chonchi, kunja mu bwalo la ng'ombe uko, tsiku lonse. Ndipo anthu amenewo anali kumeneko naini koloko mmawa umenewo, atakhala mu mvula. Ndipo mkazi ali ndi mwana wakufa m'manja mwake. Mwanayo anali atamwalira usiku wa dzulo lake, ndipo mwana wamng'onoyo atagona atawuma, m'manja mwake. Mnyamata anali atapereka makadi apemphero, ndipo anali atawapereka iwo onse. Panalibenso makadi ena apemphero. Iwo ananditsitsira ine pansi pa chingwe, kumbuyo kuseri kwa bwalolo, kuti ndilowe mu bwalomo monga chonchi. Ndipo Billy anabwera akuthamangira kwa ine. Iye anati, “Adadi, sindikudziwa kuti ndichite chiyani.” Iye anati, “Ndiri ndi othandizira firii handiredede ayimirira pamenepo.”

⁸ Ndipo ndi angati akumudziwa Jack Moore? Pafupifupi nonse a inu mukumudziwa Jack Moore, pano, ine ndikuganiza. Iye anali ndi ine.

⁹ “Ndipo kuli mkazi wamng'ono kunja uko,” iye anati, “amene ali ndi mwana wakufa, wamwalira mmawa uno.” Apo panali pafupifupi naini koloko usiku umenewo. Anamwalira m'mawa umenewo mu ofesi ya dokotala. Ndipo anati, “Iye akufuna kuti mwana wakufayo abweretsedwe mu mzere.” Anati, “Ine ndiliba makadi enanso, ndipo ine ndafoletsa mzerewo.” Anati, “Ine sindikudziwa. . .” Ndipo mvula ikuvumba mwamphamvu basi; atangoyima pamenepo mu iyo, mvula yozizira. Ndinayang'ana

kunja uko, ndipo akazi aang'ono achi Mexico amenewo, tsitsi lawo likulendewera pansi, litangonyowa, litanyowa, pansi pa magetsi amenewo. Ndipo iwe sukanatha kuwona kumeneko, mopyola, ikuvumba mwamphamvu kwambiri. Chabwino, ine ndinati. . . "Chabwino," iye anati, "Ine ndikulephera kumugwira iye," anati, "ife tiri—ife tiri ndi othandizira firii handiredede." Anati, "Iye akumakwera pamwamba pomwe pa iwo, ndipo iye wanyamula mwana wakufa uyu."

¹⁰ Ine ndinati, "Chabwino, M'bale Moore, bwanji inu osangopita uko ndi kukamupempherera iye?" Ndipo ine ndinali ndikulalikira pafupifupi kwa maminini teni, ine ndikuganiza, chinachake. Ndipo ine ndinati, "Bwanji inu osapita kukamupempherere iye," ine ndinati, "chifukwa iye sangadziwe amene ine ndiri, kapena aliyense; pakhala pali oyankhula angapo." Ine ndinati, "Iye sakudziwa kuti ine ndi ndani. Inu mupite kukamupempherere mwanayo ndipo izo zimukhutitsa iye."

¹¹ Iye anati, "Chabwino, M'bale Branham." Iye anayamba kunyamuka pa nsanja.

¹² Ndipo apo panali mulu wa zovala zakale, wotalika *motero*, njira yonse kwa, oh, mwinamwake mayadi twente kapena sarte. Bambo wakhungu anali atayamba kuwona, usiku wadzulo lake, ndipo kotero iwo anali okondweretsedwa kwenikweni. Nainte peresenti Achikatolika.

¹³ Kotero ine ndinayamba kulalikira. Ine ndinati, "Monga ine ndimanenera, chikhulupiriro ndi chi- . . ."

¹⁴ Ine ndinayang'ana, atayima patsogolo panga, ndipo apo panali mwana wamng'ono wachi Mexico; nkhope yaing'ono yakuda, nkhamazazing'ono, zopanda mano, zikungonyezimira, nkhamazazing'ono monga choncho. Ndipo ndinaganiza, "Ameneyo akuyenera kukhala mwana uja." Ine ndinati, "Dikirani miniti, M'bale Moore. Muuzeni dona wamng'onoyo kuti amubweretse mwanayo kuno."

¹⁵ Kotero iwo anamutsegulira, mchipindamo; wopanda—wopanda khadi la pemphero. Iye sankayenera kulowamo kwenikweni, koma anakakamira. Ndizo—ndizo zomwe inu mumafuna. Kotero iye anamubweretsa mwanayo.

¹⁶ Ine ndinati, "Atate Akumwamba!" Ndithudi, iwo samatanthauzira pemphero. Ine ndinati, "Sindikudziwa ngati uyu ali mwanayo, kapena ayi. Ine ndangomuwona mwana wamng'ono. Koma ngati ali uyu, ndi ulemu Wanu kwa mkazi uyo yemwe akupanga nsembe iyi." Ine ndinasanjika manja anga pa bulangeti la buluu limenelo, ndipo kanthu kowuma kakang'onoko kotalika *chomwechi*, kakulendewera mu nkono wa mkaziyo.

¹⁷ Ndipo mwanayo anafuula ndipo anayamba kukankha, pamwamba pake. . . akungofuula mwamphamvu momwe

akanathera. Mwanayo anali...Tsopano dona wamng'onoyo anagwera pansi ndikuyamba kukuwa, "Padre!" *Padre* amatanthauza "atate," inu mukudziwa. Anali ndi mikanda m'manja mwake.

Ine ndinati, "Izo sizofunikira."

¹⁸ Ndipo ine ndinanena kwa M'bale Espinoza, mlaliki wa Chipentekoste. Ambiri, ine ndikuganiza, ine ndikuganiza inu mukumudziwa iye. Eya, M'bale Espinoza. Ine ndinati, "Tsopano inu musalembe, 'mwanayo anali atafa.' Ine sindikudziwa. Chinthu chokha chimene ine ndinachiwona chinali chakuti panali, masomphenya amenewo." Ine ndinati, "Inu mutumize a—wothamanga amutsatire mkazi ameneyo, ndipo mumusiye iye apite ndikukawalola adokotala kuti akalembe chikalata cha zimenezo."

¹⁹ Ndipo a Christian Business Men's *Voice* posakhalitsapa analemba nkhanayo, "Dokotala wapereka umboni, 'mwanayo anamwalira ndi chibayo chowirikiza kawiri,' mu ofesi yake m'mawa umenewo, 'pa kota kuti ikwane naini koloko.'" Ndipo imeneyo inali teni koloko usiku umenewo, Ambuye Yesu anamupatsanso iye moyo wake kenanso, chifukwa cha nsembe. Tsopano, izo ndi zoonza kwambiri! Mulungu Kumwamba akudziwa kuti izo ndi zolondola. Chikalata chotsimikiziridwa cha dokotala! Chikalatacho tsopano chiri mmanja mwa a Christian Business Men, omwe Demos Shakarian ndi... mtsogoleri wawo wapadziko lonse. Iye ali ndi chikalatacho chosayinidwa ndi dokotala, "Mwanayo anamwalira ndi chibayo chapawiri, mmawa umenewo." Ndipo teni koloko usiku womwewo mwanayo anakhalanso moyo, chifukwa cha chikhulupiriro cha mayi amene anali wokakamira kuti achite izo. Ndi choncho.

²⁰ Chimodzimodzi basi monga momwe mkazi wamng'ono wa ku Shunemu anakakamirira kuti akafike kwa Eliya!

²¹ Chimodzimodzi basi monga Mgriki, mkazi wa ku Surofonika anakakamira kuti akafike kwa Yesu. Iye ankadziwa kuti anali ndi mwana wamkazi amene anali ndi khunyu. Ngakhale, kuti iye sanali Myuda nkomwe. Chitsitsimutsocho sichinali cha anthu ake. Ndipo kenako pamene Iye anafika, iye anafika kwa Iye, Iye anati, "Sikoyenera kwa ine kuti nditenge mkate wa ana ndi kuwupereka kwa agalu." Anamutcha iye galu.

²² Iye anati, "Izo nzoona, Ambuye." Mwaona momwe chikhulupiriro chenicheni chingachitire umboni Mawu kukhala Choonadi! "Zoonadi, Ambuye, koma agalu ndi lolera kudya nyenyetswa pansu pa gome la mbuye wawo."

²³ Iye anati, "Chifukwa cha mawu awa, mwana wako wachiritsidwa." Ndipo iye anapeza izo mwanjira yomweyo, chifukwa iye anali wokakamira.

²⁴ Zikomo, kwambiri, abwenzi. Ambuye amudalitse aliyenseyo, azing'wenyeng'wenye, Mlongo Ungren apa, ndi abwenzi anga onse. Ine ndikuwona apa kuti ambiri a azimzanga abwera ku msonkhano uwu. Ine ndawawona, lero, M'bale ndi Mlongo Evans. Ine sindikudziwa ngati iye angakhoze nkomwe kundimva ine, kapena ayi. Iwo ndi ochokera uko ku Macon, Georgia. Mlongo Ungren pano ndi—ndi onse a iwo ochokera uko ku Memphis, Tennessee. Ndi M'bale Palmer ndi Mlongo Palmer, ndi azimzawo. Ndi M'bale Parnell, mtumiki mzanga kumeneko. Ine ndikuwawona iwo angokhala mozungulira pano tsopano, azimzanga, azimzanga apadera. M'bale J. T. pano, wochokera—wochokera uko ku Georgia, nayenso, bwenzi wake. Ndipo ndithudi ndife othokoza kukhala nanu nonse pano, ndi chikhulupiriro chanu ndi chidaliro. Ena a anthu amenewo amayendetsa mpaka ku Jeffersonville, Indiana, Lamlungu lirilonse limene ine ndikulalikira kumeneko, kungobwera kumeneko kuti adzamvetsere. Ndiye ine ndikukuuzani inu, kuti, dziko siloyenera anthu oterowo, mwa lingaliro langa. Ameneyo ndi ine ndikuganiza zimenezo. Anthu inu pano, ndife gulu limodzi lalikulu la Khristu. Ife timakhulupirira mwa Iye.

²⁵ Ndipo tsopano uwu sungakhale msonkhano pokhapokha ine nditatenga maminiti pang'ono kuti ndiwerenge Mawu ndi kupereka ndemanga zingapo. Chifukwa, ngati inu mwakhala okhulupirika mokwanira kudzakhala pano motalika chomwecho, ine ndikufuna kukhala wokhulupirika mokwanira kwa izo, kuti ndiwerenge Lemba ndi kupereka ndemanga chabe kapena ziwiri, ndipo kenako ife tiyambitsa mzere wa pemphero.

²⁶ Tsopano ine ndiwerenga lero kuchokera mu Lemba, kuchokera ku Marko mutu wa 16, kwa mphindi pang'ono chabe, kuti nditenge phunziro kuchokera mu nkhani iyi. Ndiyambira pa ndime ya 14.

Ndipo atatha kuwadzudzula iwo, *kwa leveniwo... anawonekera kwa leveniwo pamene... atakhala pachakudya, ndipo anawadzudzula iwo chifukwa cha kusakhulupirira kwawo ndi kuuma mtima kwawo, chifukwa iwo sanawakhulupirire iwo amene anamuwona iye atatha kuwuka.*

...iye anati kwa iwo, Pitani inu mdziko lonse lapansi, ndipo mukalalikire uthenga kwa cholengedwa chirichonse.

²⁷ Tsopano kumbukirani, “Ku dziko lonse, Uthenga uwu, kwa cholengedwa chirichonse.” Ena amati Iwo unatha ndi atumwi. Iye ananena apa, kuti, kutuma Kwake kotsiriza kwa Mpingo, kunali, “Ku dziko lonse, kwa cholengedwa chirichonse. Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Kuti? “Ku dziko lonse, kwa cholengedwa chirichonse.” Zindikirani,

apo ndi pamene Iye anapereka izo kwa Mpingo; ndisonyezeni ine pamene Iye anachotsa izo. Uh-huh. “Dziko lonse lapansi!”

Iye amene adzakhulupirira . . . adzapulumutsidwa; . . . iye amene sadzakhulupirira adzawonongedwa.

Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira; Mu dzina langa iwo adzatulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime atsopano;

Iwo adzanyamula njoka; . . . ngati iwo adzamwa chinthu chakupha chirichonse, icho sichidzawavulaza, sichidzawapweteka iwo; iwo adzayika manja awo pa odwala, ndipo iwo adzachira.

Kotero . . . Ambuye atatha kuyankhula kwa iwo, iye analandiridwa kumwamba, ndipo anakakhala pa dzanja lamanja la Mulungu.

Ndipo iwo anapita, . . . akulalikira konsekonse, Ambuye akugwira ntchito ndi iwo, . . . akutsimikizira mawu ndi zizindikiro zikuwatsatira. Amen.

²⁸ Tsopano, ine ndimakhulupirira Lemba limenelo kuti ndi Choonadi.

²⁹ Ndisanaiwale izo, mwana wanga amandiuza ine kanthawi kapitako, dona wina wamng’ono, ndi mwamuna wake ochokera ku Arkansas, anandiphikira keke ya tsiku lobadwa ndipo adzandipatsa ine. Ambiri a inu mwandipatsa ine makadi ndi zinthu. Sindinakhale ndi nthawi nkomwe yoti ndilowe mu izo. Zikomo, kwambiri. Mulungu akudalitseni inu. Ndipo ndikuyembekeza kuti inu muli ndi . . . ife tonse tidzakhala ndi tsiku lobadwa Lamuyaya kutsidyako, kumene tidzakhale pansi, ndipo ine ndikufuna a—Ine ndikufuna zaka teni sauzande ndiri ndi aliyense wa inu, kudzangokhala pansi ndi kumayankhulana. Ndipo ife sitidzakhala ndi nthawi yochepa iriyonse, yocheza, kuposa pomwe tinayambira. Icho ndi Choonadi. Tsopano ndikukuthokozani inu chifukwa cha zonse zomwe mwachita.

³⁰ Tsopano kwa pafupifupi maminiti teni okha, kapena fifitini mopambana, mwinamwake, ngati Ambuye alola, kuti ndingopereka ndemanga pang’ono.

³¹ Ine ndikufuna kuti ndinene ichi, kuti ine ndikudalira kuti kumverera kwanga, kotsogolera kuti ndibwere; azibusa inu kumverera kutsogozedwa kuti mundithandizire ine kuti ndibwere, zimenezo zinandipatsa ine khomo lotseguka; anthu inu munali okhulupirika kutulukako; ndipo Yesu sanalephere koma Iye wakhala akuwonekera kwa ife nthawi iliyonse, mu chizindikiro cha ora limene ife tikukhalamo. Ndipo ine ndikudalira kuti chiwukitsiro Chake, chosatha, Umunthu Wamuyaya, ndi Kukhalapo Kwake, zakulimbikitsani kuti mumukonde Iye ndi kumutumikira Iye kuposa mmene munayamba mwachitirapo m’moyo wanu wonse, kulinga

mu mtima mwanu kuti mukhale moona kwa Iye, ndi kukhala momuyandikira, mwabwinoko.

³² Ine ndinamvapo nkhami imene inakambidwa kwa ine, ya pamene iwo anali ndi akapolo kuno Kummwera.

³³ Iwo ankakonda kuwagulitsa iwo pa misika, ndi zina zotero, monga iwo ankachitira mu nthawi ya akapolo. Iwo, ma Bunu, ankawabweretsa iwo, kunja kuno ku Jamaica Island. Kenako anthu cha kuno, ankawazembetsera iwo mkati. Ndipo iwo ankawagula iwo kukhala akapolo, chimene chinali chololedwa mmasiku amenewo. Ndipo ankapita ndi kukawagula iwo, ndipo iwo ankapeza akapolo abwino ojintcha, bwanji, iwo anka... Iwo ankatha kumukweranitsa kapolo wamkulu wojintcha uja kwa mkazi wojintcha; izo zinkapanga munthu wabwinoko. Ichonchi chifukwa chake iwo ali ngwazi za mdziko lero, mu zinthu, mu kumenyana kwawo. Iwo basi ankangokweranitsa, ngati ng'ombe, ndi zina zotero.

³⁴ Koma ndiye tikumupeza wogula, nthawi yina, wogula anabwera kudzagula pamunda pamene iwo anali ndi akapolo pafupifupi handiredede.

³⁵ Ndipo akapolo amenewo, anali, iwo anali omvetsa chisoni. Iwo ankachita kuwakwapula iwo, kuti awapangitse kugwira ntchito, chifukwa iwo anali kutali ndi kwawo. Iwo ankachita kuthawitsidwa, amawagwira, nkupita ku ukapolo ndipo amathawitsidwira kutali. Ndipo ankachita kumawakwapula iwo, kuti awapangitse iwo kugwira ntchito, chifukwa iwo amakhala okhumudwitsidwa; iwo anali kutali ndi kwawo. Iwo sadzawawonanso abambo ndi amayi. Sadzawawonanso akazi awo kapena ana awo. Zinali zomvetsa chisoni.

³⁶ Ndipo wogula uyu, tsiku lina, anabwera pa mundawo, anati, “Kodi muli ndi akapolo angati?”

Anati, “Pafupifupi handiredede.” Anati, “Ayang'aneni iwo.”

³⁷ Ndipo iye anapita kunja uko, ndipo anakawawona iwo, momwe iwo onse analiri... Koma mnyamata mmodzi wamng'ono, iwo sankasowa kuti amukwapule iye. Chidale chake chimakhala panja. Chibwano chake chimakhala mmwamba, pa malo ake. Ndipo kotero wogulayo, wogulayo, anati kwa mwiniwakeyo, iye anati, “Ndikuti, ndikufuna kugula kapolo ameneyo.”

Iye anati, “Oh, ayi. Iye si wamalonda.”

³⁸ Iye anati, “Chabwino,” anati, “kodi ameneyo ndi kapolo, iye ndi bwana wa ena onsewo?”

Iye anati, “Ayi, ayi, iye si bwana.”

Anati, “Kodi inu mumamudyetsa iye mosiyana?”

³⁹ Anati, “Ayi. Iwo onse amadya kunja uko mu ngalande, pamodzi. Iye ndi kapolo basi.”

Anati, “Chikumupangitsa iye kukhala wosiyana kwambiri ndi ena onsewo ndi chiyani?”

⁴⁰ Iye anati, “Ine ndinakhala ndikudabwa kwa nthawi yayitali, inemwini, chimene chimamupangitsa iye kukhala wosiyana. Koma tsiku lina ndinazindikira. Uko ku dziko la kwawo, kumene iwo anachokerako, ku Africa, abambo ake ndi mfumu ya fuko. Ndipo komabe, pokhala mlendo, iye amadziwa kuti ndi mwana wa mfumu, ndipo amachita monga mmodzi.”

⁴¹ Oh, kodi zimenezo zikuyenera kuchita chiyani kwa ife! Ngakhale ife tiri alendo, ngakhale ife tiri mdziko lamdima la kusakhulupirira, ndi chisoni ndi matenda ndi imfa, komabe tiyeni tizichita monga ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ife ndi ana aamuna ndi aakazi a Mfumu. Izo zikuyenera kusintha kaganizidwe kathu, chirichonse. Ziribe kanthu chimene dziko lonse lapansi liri, ife tikuyenera kugwiritsitsa maufulu a Mulungu. Tizikumbukira kuti kuno si kwathu. Ife sitiri a mdziko lino. Sindife a mdziko lino. Ndife obadwa mwa Mzimu wa Mulungu, umene uli Kumwamba.

⁴² Ndikupita, ndi mkazi wanga, kuno osati kale litali, ku golosale. Ine ndinawona chinthu chachirendo mu nthawi ya chirimwe, mu Indiana, mkazi anali atavala diresi. Iwo sakumavala iwo panonso, inu mukudziwa. Ndipo kotero, mkazi wanga anati. . . Ine ndinati, “Chabwino, tayang’ana apo! Ndikudabwa ngati mkaziyo ali Mkhristu.”

⁴³ Iye anati, “Chabwino, akazi onsewa; Ndikuwadziwa ena a iwo kuno, iwo amayimba mmakwaya mmatchalitchi.” Iye anati, “Kodi nchifukwa chiyani, Bill, iwo akumachita zimenezo?” Ine ndinati, ndithudi. . . “Ndipo—ndipo anthu athu samachita zimenezo.”

Ine ndinati, “Ndithudi. Ndife a fuko losiyana.”

Iye anati, “Ife ndi Achimereka, sichoncho ife?”

⁴⁴ Ine ndinati, “Oh, ayi. Ife tangomanga msasa kuno. Ife sitiri Achimerika.” Ine ndinati, “Mwaona, ndife ochokera Kumwamba.”

⁴⁵ Mzimu Woyera unatsika, unalumikizitsa mitima yathu ndi Mulungu, ndipo ife tinadzinenera, monga Abrahamu, “Ndife amwendamnjira ndi alendo.” Kuno si kwathu. “Ife tikufunafuna mzinda Umene wowumanga ndi wowupanga wake ndi Mulungu,” kuchokera Kumwamba. Inde, ndife ana aamuna ndi aakazi a Mfumu.

⁴⁶ Tsopano ndibweretsa chinthu chaching’ono chimene chikumveka moseketsa, kwa maminiti pang’ono chabe, koma ine ndikhala ndi mlandu, mlandu wa m’khoti apa.

⁴⁷ Inu mukundimva ine? Mpaka pati kumbuyoko mukukhoza kundimva ine, kwezani manja anu. Chabwino, ziri bwino.

Kumbuyo mbali *iyi*, inu mukundimva ine? Zabwino. Ine ndikuyankhula mokweza, pafupifupi, momwe ndingathere.

⁴⁸ Ine ndikhala ndi mlandu waku khoti, ndipo mlanduwu ndi wakuti: *Mawu a Mulungu, Olonjezedwa akutsutsana Ndi Dziko*. Tsopano ife tiziyika izo ngati mlandu waku khoti kwa kanthawi pang'ono chabe, inu musanadutse mzere wa pemphero uwu. *Mawu a Mulungu kutsutsana ndi Dziko*.

⁴⁹ Tsopano, mlanduwu, choyambitsa cha chitsutsochi ndi kuphwanyanya kwa lonjezo, ndi chakuti, “Malonjezo a Mulungu,” iwo amanena kuti, “Mulungu sanasunge lonjezo Lake.”

⁵⁰ Wosuma mlandu pa mlanduwu ndi Satana, ndipo iye ndi mboni ya dziko lapansi, chifukwa iye ndi wa mdziko lapansi.

Woyimbidwa mlandu pa mlanduwu ndi Mulungu Wamphamvuzonse.

Mboni ya woyimbidwa mlanduwu ndi Mzimu Woyera.

Ife tiwayitanira iwo ku mlandu, kwa maminiti pang'ono chabe.

⁵¹ Mboni za wosuma mlandu, zomwe iye akuzibweretsa kuti zidzateteze mlandu wake, ndi Bambo Kusakhulupirira, Bambo Kukayikira, ndi Bambo Kusapirira.

⁵² Ife tiwapatsa iwo mlandu. Khoti likufunsidwa likhale mu dongosolo tsopano. Wosuma mlandu akuyitana mboni yake, Bambo Kusakhulupirira. Iye akutenga malo ake, poyamba.

⁵³ Kodi mukundimvabe ine? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino. Zabwino. Tsopano ine ndikumverera kumasukako pang'ono.

⁵⁴ Tsopano, inu mukumvetsa, uwu ndi mlandu womutsutsa Mulungu, umene Bambo Kusakhulupirira ndi Bambo Kukayikira ndi Bambo Kusapirira akumuyitanira Mulungu ku—ku mlandu, “chifukwa Iye samasunga Mawu Ake,” iwo amatero. Chabwino.

⁵⁵ Woyimira mlandu pa nkhani *iyi*, iye nthawizonse amayimira boma, kotero woyimira mlandu kumbali yosuma mu boma limeneli ndi Satana mwiniwake. Ndipo iye ndi . . .

Ife tikuyitanitsa mlandu.

⁵⁶ Chabwino, iwo akuyitanira woyambayo pa malo ochitira umboni, ameneyo ndi Bambo Kusakhulupirira. Iye akudandaula izi, kuti, “Mawu onse olonjezedwa a Mulungu si owona.”

⁵⁷ Tsopano Iye ayesedwa pa izi. Mvetserani mwatcheru tsopano. Musaphonye zimenezo.

⁵⁸ Iye akunena kuti Marko 16, yemwe ndangowerenga kumene, anatumikiridwapo kwa iye mu umene unkatchedwa kuti msonkhano wa Mzimu Woyera kumene ena ankadzinenera kuti akuchiritsidwa. Ndipo izo zinatumikiridwa kwa iye, zaka ziwiri zapitazo, ndipo palibe kusinthika mwa iye panobe, kuti,

“Izi ‘zizindikiro’ sizimamutsatira wokhulupirira.” Iye anati iye anapanga kudzinenera uku motsutsa Iwo. Chabwino, iye wakhala pansi.

⁵⁹ Tikuyitana mboni yotsatira. Ameneyo ndi Bambo Kukayikira. Iye akutenga Lemba la Mawu a Mulungu, la Yakobo 5:14. Ndipo iye anati anali pamalo pamene iwo anati akulu anayitanidwa, ndipo iye anadzozedwa ndi mafuta ndipo anapemphereredwa. Ndipo izo zinali kupitirira mwezi wapitawo, ndipo sipanakhale kusintha mwa iye panobe, kotero iye akudziwa kuti izo nzolakwika. Iye akumuyitana Mulungu, ndi kumutsutsa Mulungu, chifukwa cha zimenezo.

⁶⁰ Mboni yotsatira ndi Bambo Kusapirira. Iye ndi munthu woyipa. Chabwino. Bambo Kusapirira, iye akunena kuti anawerenga Mawu a Mulungu, pa Marko 11:22 ndi 23, kuti pamene mupemphera, ngati mukhulupirira kuti chimene mwapemphacho, mwalandira, inu mukuyenera kulandira chimene mwapemphacho. Ndipo iye ananena kuti iye anapempha kuti ayike pansi ndodo zake, iye atatha kuwerenga Mawu ndi kumupempha Mulungu kuti amuchiritse iye. Ndipo anapempha kuti ayike pansi ndodo zake, ndipo zimenezo ndi zaka faivi zapitazo, ndipo iye sanayambe wakwanitsapo kuziyika izo pansi kuyambira pamenepo.

⁶¹ Kotero iwo—kotero iwo amati, “Mulungu samalungamitsidwa poyika malonjezo achangu oterowo m’Mawu Ake.” Tsopano kodi inu mukuwumvetsa mlanduwu tsopano womutsutsa Mulungu? “Iye samalungamitsidwa pochita zimenezo, powayika Malemba oterowo monga Marko 11:23, 22 ndi 23, ndi Marko 16, Yakobo 5:14, ndi malonjezo oterowo monga amenewo.” Iwo akumutsutsa Mulungu chifukwa cha kuphwanya lonjezo, kuti, “Iye waphwanga lonjezo Lake, ndipo sakutha kuyima nalo.” Ndipo iwo akumutsutsa Iye chifukwa choyika zoterozo mu Mawu Ake, pakuti, “Ana ake okhulupirira samadziwika ndi zodzinenerazo, ndipo zimawachititsa iwo kuti azunzidwe, chifukwa si ali...Mulungu samawazindikitsa Mawu Ake Iye atatha kupanga lonjezo.”

⁶² Oh, ife tiri ndi mlandu weniweni apa tsopano. Ine ndikuyang’ana pa iwo, momwe iwo achitire umboni! Komabe, imvani mbonizo zikuyimiranso kachiwiri ndipo zikunena kuti, “Komabe, ife ndi okhulupirira!” Iwo akudzinenera kuti ndi okhulupirira, iwoeni. “Ndipo anati, ‘Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.’ ‘Pemphero lachikhulupiriro lidzapulumutsa odwala.’ ‘Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, “suntha” ndipo osakayikira mumtima mwanu, izo zidzachitika. Ndipo ife ndi okhulupirira.” Ndipo, komabe, kenanso wina akuyimirira ndikuti, “Komabe, Iye, ameneyo ndi Mulungu, analonjeza kuti zinthu zonse nzotheka kwa okhulupirira.” Ndi chitsutso chotani kwa Mulungu ndi Mawu Ake!

⁶³ “Komabe, aponso, Iye amadzinenera kuti ndi wamoyo Iye atatha kupachikidwa. Ndipo amadzinenera kuti Lembu Lake pa Ahebri 13:8, kuti Iye ndi Mulungu mochuluka basi lero monga Iye analiri dzulo, ndipo adzakhala kwanthawizonse.” Tangoganizani za Mulungu yemweyo! Ndipo iwo akumutsutsa Iye chifukwa cha izo, chifukwa, “Izo siziri chomwecho,” iwo sakuzipanga izo kukhala zolondola. Chabwino.

⁶⁴ “Komanso, kuti Iye amadzinenera,” uyu ndi wodandaulayo tsopano, “Iye amadzinenera kuti zonse kumwamba ndi dziko lapansi zidzalephera, koma Mawu Ake sadzalephera konse.” Iwo akuyenera kukhala okhulupirira akuyankhula. Tsopano, ndi mlandu wotani! Ndi dandaulo lotani limene ife tiri nalo lomutsutsa Mulungu, kuti, “Iye ananena maneno awa, ndipo osakhala wamkulu mokwanira kuti awayimire kumbuyo kwake.” Inu mukuganiza chiyani za zimenezo?

⁶⁵ Ndipo Satana wosuma mlandu atakhala pamenepo, akuliyimirira dziko, kudzanena izi, kuphwanya kwa lonjezo kwa Mulungu, chifukwa, “Anthu awa abwera, akhala ali mmisonkhano iyi, ndipo—ndipo avomereza zinthu izi zimene Mulungu ananena, kuti ndi zolondola, ndipo komabe palibe chimene chachitika kwa iwo.”

⁶⁶ Tsopano, tsopano tiyeni tilole mboni za wosuma mlandu zitsike kwa miniti yokha, inu mukudziwa. Iwo ali ndi mbali yina.

⁶⁷ Tsopano tiyitana mboni ya woyimbidwa mlandu. Mboni yodzitchinjiriza ya woyimbidwa mlandu, ameneyo ndi Mulungu. Mboni yotetezera mlandu ya Mulungu ndi Mzimu Woyera. Mubweretseni Iye pamalopo. Tiyeni timve umboni Wake.

⁶⁸ Mai! Choyamba, Iye akuyitanira tcheru ku kutanthawuzira kolakwika kwa Mawu kwa wosuma mlandu kwa anthu. “Uko nkulondola, pakuti iye ndi wotanthawuzira yemweyo amene Eva anali naye. Iye ndi wotanthawuzira yemweyo amene Eva anali naye. ‘Oh, ndithudi, *Ich*i kapena . . . *Ich*i ndi chabwino, koma *Ich*o sichiri.’ Mwaona, wotanthawuzira yemweyo, ndi yemweyo wosuma mlandu, chifukwa iye ndi mdierekezi. Yemweyo amene . . .”

⁶⁹ Mulungu ankawamangira linga ana Ake kuseri kwa Mawu Ake. Ndipo nthawi yoyamba yomweyo imene inu muchoka kuseri kwa Iwo, inu mumakhala chandamale cha mdierekezi. Koma iye sangakupezeni inu bola ngati muli ndi linga la Mawu.

⁷⁰ “Tsopano lonjezo liri . . .” Iye ananena kenanso, “Ndikufuna kuyitanira tcheru chanu.” Akuti . . . Tsopano iyi ndi mboni ya woyimbidwa mlandu, Mzimu Woyera. Iye anati, “Lonjezo liri kwa okhulupirira okha, osati odzipangitsa kukhulupirira ndi okayikira ndi osakhulupirira. Lonjezo liri kwa okhulupirira okha, osati kwa enawo.” Tsopano, uyu ndi—iyi ndi mboni ya oyimbidwa mlandu. Ndipo mboni ya woyimbidwa mlandu

ikuyenera kudziwa, chifukwa Iye ndi amene amafulumizitsa ilo kwa iwo. Iye amadziwa ngati izo ziri zoonza kapena ayi.

⁷¹ Iye akufunanso kuyitanira tcheru apa, pokhala wofulumizitsa Mawu, Iye akuyitaniranso tcheru, kuti, “Mawu ndi mbewu. Ndipo ngati mbewuyo igwera mu nthaka yoyenera, yachonde, iyo idzabala ndendende chimene Mulungu ananena kuti ikanadzachita. Koma iyo sinagwere mu nthaka yoyenera, kotero mulibe dothi lokwanira, chikhulupiriro chokwanira, chopangitsa mbewuyo kukula.” Ine ndikuganiza, monga Mmodzi Amene amafulumizitsa mbewu, Iye akuyenera kudziwa. Kodi inu simukuganiza choncho? Ndi angati akukhulupirira zimenezo? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Iye akuyenera kukhala Mmodzi Amene akudziwa. Iye ndi mboni yeniyeni ya woyimbidwa mlandu. Chabwino.

⁷² Woyimbidwa mlandu, akuchitira umboni tsopano, ayitana mboni Yake yoyamba. Tsopano, inu mwaona, wosuma mlandu anayitana mboni yake, Bambo Kusakhulupirira, Bambo Kukayika, ndi Bambo Kusapirira. Tsopano mboni ya woyimbidwa mlandu ili ndi ufulu woyitana imodzi mwa mboni Zake. Mzimu Woyera uli ndi ufulu woyitana iyo, chifukwa Iye ndi mboni ya woyimbidwa mlandu ya Mawu a Mulungu.

⁷³ Tsopano, amuna awa akunena kuti amakhulupirira, koma Mzimu Woyera sunadziwe kalikonse za izo, ndipo Iye ndi mmodzi yekhayo amene angakhoze kuwafulumizitsa Iwo. Ziri ngati thupi lanu pano, mwaona, thupi lanu ndi lakufa popanda mzimu, chomwechonso Mawu a Mulungu ali akufa popanda Mzimu Woyera kuti uwafulumizitse Iwo. Mzimu umafulumizitsa thupi, ndipo Mzimu Woyera umafulumizitsa Mawu. Inu mukumvetsa zimenezo? Tsopano, Iye akuyenera kudziwa.

⁷⁴ Tsopano Iye ayitana mboni yoyamba. Tiyeni tiwone amene Iye ati amuyitane. Nowa, Iye amuyitana Nowa.

⁷⁵ Nowa anati, “M’masiku amene ine ndinakhalamo unali m’badwo wasayansi,” anzeru kwambiri kuposa momwe iwo aliri mu tsiku lino. “Ndipo Ambuye Mulungu anandiuza ine kuti ivumba mvula kuchokera kumwamba.”

⁷⁶ Iyo inali isanavumbepo, inu mukukumbukira, pa dziko lapansi. Ndipo iwo ankakhoza kutenga zida ndi kutsimikizira kuti munalibe mvula mmwamba mmenemo. Kumbukirani, inali isanavumbepo mmasiku amenewo. Mulungu ankathirira dziko lapansi kudzera mu kathirira.

⁷⁷ Koma iye anati, “Iyo ivumba ndipo iwononga dziko lapansi. Padzabwera chigumula chachikulu, pa dziko lonse, chimene chidzaphimbe ilo ndi kuliwononga ilo.” Iye anati, “Komabe, ine ndiri ndi malamulo ochokera kwa Mulungu, kuti ndimange chombo. Ine ndinapita kukagwira ntchito pa chombo ichi, kuwonetsera chikhulupiriro changa, kuti ine ndinkakhulupirira

kuti chimene Mulungu ananena chinali Choonadi, mosalabadira zomwe sayansi inkanena za izo.” Ndikuganiza kuti iye ndi mboni yabwino, sichoncho inu? “Ndipo ziribe kanthu zomwe wina aliyense akunena za izo, Mulungu wanena kuti iyo ivumba; kotero ngati simunayambe mwakhalapo mvula m'mwamba umo, Iye akhoza kuiyika mvula mmwamba mmenemo. Ine ndimanga chombo, mulimonse, kuchikonzeke retsa icho.

⁷⁸ “Ngakhale, ine ndinali ndi munthu ameneyo, pa nsanja yochitira umboni apa kanthawi kapitako, Bambo Kusakhulupirira, iye ankandinyoza ine nthawi yonse. Iye ankandiseka ine. Ndipo ine ndinawawona Bambo Kukayika; iwo anabwera ndipo anadzandiseka ine. Bambo Kusapirira, onse a iwo, ankandiseka ine, chifukwa chokhulupirira chozizwitsa choterocho. Koma, ine ndinadikirira. Nditamaliza chombocho, mvula siyinabwere. Ndipo ine ndinayembekezera kwa zaka wani handirede ndi twente, iyo isanabwere, koma iyo inadzabwera.” Amen.

⁷⁹ “Khala pansi, mboni. Umenewo ndi umboni wabwino. Tiye tiyitane ina, mboni yachiwiri. Abrahamu, m'bweretseni iye.” Iye takhala tikuyankhula za iye.

⁸⁰ “Nayenso,” iye anati, “Ndinamva Mawu a Mulungu, pamene ine ndinali wa zaka sevend-faivi zakubadwa, anandiwuza ine chinachake chimene chinali mwamtheradi chotsutsana ndi kulingalira konse. Ichu chikanayenera kukhala chozizwitsa chapamwamba kuchulukitsa chapamwamba. Kuti, ine ndinali woti ndikhala ndi mkazi, wa usinkhu wa zaka sikisite-faivi, kuti andiberekere ine mwana wamwamuna pamene iye anali wa usinkhu wa zaka sikisite-faivi. Iye tinapita kumusi ndi kukakonzekera chirichonse, chifukwa Mulungu ananena choncho. Iye tinazikhulupirira izo. Ndipo a... Ndinawauza azimzanga onse kuti zinthu izi zikanadzachitika pambuyo... Izi zinkayenera kuchitika chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Ine ndinadikirira moleza mtima. Mwezi woyamba unafika, ndinamufunsa mkazi wanga kuti akumverera bwanji. ‘Palibe kusintha.’ Chabwino, ine ndinamukhulupirira Mulungu, mulimonse.

⁸¹ “Apo panali Bambo Kusakhulupirira, Bambo Kunyoza, Bambo Kukayikira, ndi onse a iwo atayima mondizungulira. Iwo ananyoza ndi kumandiseka ine, ankanditcha ine, ‘Atate wa mafuko,’ pamene ndinalibe ana.

⁸² “Ndipo ndinapitirira kukhulupirira mwezi uliwonse, mwezi uliwonse izo zichitika. Iye anakalambira ndi kukalambirabe nthawi zonse, koma izo... mu zaka twente-faivi mtsogolo, Mulungu anasunga Mawu Ake kukhala owona. Izo zinadzachitika.”

⁸³ “Abrahamu, umenewo ndi umboni wabwino. Mawuwo sananene kuti *liti*; Iye anati Iye akanadzatero. Iye anati, ‘Ine

ndidzakupatsa iwe mwana, wamwamuna, mwa Sarah.’ Osati mwezi wotsatira; Iye sananene konse kuti mwezi wamawa. Iye anati Iye akanadzatero; osati *liti*. ‘Pemphero...’ ‘Iwo adzayika manja pa odwala, iwo adzachira.’ Limenelo ndiro ganizolo. ‘Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwala, ndipo Mulungu adzamuukitsa iye.’ ‘Dikirani inu mu mzinda wa Yerusalemu mpaka mutadzazidwa ndi Mphamvu, ya Kumwamba.’ Osati kwa tsiku limodzi, maora awiri, masiku teni, zaka teni. ‘Mpakana Mphamvuyo idzabwere!’” Mboni yeniyeni ya woyimbidwa mlandu, anthu awa ali! “Iye sananene kuti tidzakhala ndi mwanayo liti,” Abrahamu anatero, “koma Iye anati ife tikanadzakhala naye. Ndipo nthawi zonse zovutazo zinkandikulirakulirabe ine, ine ndinakhala wokhazikika. Chifukwa, ine sindinadzandime pa kusakhulupirira kwa anthu. Ine ndinagwiritsitsabe.”

⁸⁴ “Chabwino, Abrahamu, khala pansi. Tsopano tiyeni tikhale ndi mboni yina, mboni yachitatu. Tiyeni timubweretse Mose, tiwone zomwe iye atanene.”

⁸⁵ “Tsopano,” iye anati, “Ine ndinali wasayansi. Ndinali nditakhala kwa zaka forte mu chipululu, nditatha kulephera pa ntchitoyo. Koma tsiku lina ndinakumana ndi Mulungu. Ndipo Liwu limenelo, Lawi la Moto mmbuyo ku chipululu, linandiwuza ine, Liwu Lamalemba, kuti oralo linali pafupi, kuti Iye anamva kulira kwa anthu Ake, anakumbukira lonjezo Lake, ndipo Iye ankapita kumusi kuti akawawombole iwo, ndipo Iye ankanditumiza ine ku ntchitoyo.

⁸⁶ “Ine ndinamupempha Iye chizindikiro. Iye anandipatsa ine chizindikiro, ndipo Iye anandipatsa ine chizindikiro china; zizindikiro ziwiri zonsezo zinali ndi liwu. Iye anati, ‘Ndiye ngati iwo sakakhulupirira zizindikiro zonsezo, ukangotsanulira madzi a m’nyanja pa nthaka, iwo akasanduka magazi.’ Ndi zimenezotu, ndizo zonse za izo. Farao anathedwa pamenepo. Anati, ‘Ngati, iwe... iwo sakakhulupirira zizindikiro zimenezo, maliwu amenewo...’

⁸⁷ “Ndipo, komabe, ine ndinapita kumusi mu mzere wa ntchito, monga momwe Mulungu anandiwuzira ine kuti ndichite. Yehova, INE NDINE, anandiwuza ine kuti ndipite kumusi ndi kukachita chizindikiro ichi. Ndipo ine ndinatengera chizindikiro ichi kumusi pamaso pa m’busa Farao, ndipo ine ndinaponyera pansi ndodo yanga. Ndipo inu mukudziwa chiyani? Iye anayesera kupangitsa izo kuti ziwoneke zokayikitsa, ngati kuti iyi inali njomba yina yamatsenga. Ndipo iye anatenga onyengezera ena achithupithupi kuti atuluke ndi kukanyoza izo, kukachita chinthu chomwecho. Koma ine ndinadziwa kuti amenewo anali Mawu a Mulungu, ndipo ine ndinali nditabwera kudzawatenga ana amenewo kuwachotsa kumeneko. Ziribe kanthu chimene chinachitika, ine ndinakhulupirirabe Mawu a Mulungu, kotero ine ndinawagwira Iwo mokhazikika.” Amen!

⁸⁸ Mose, ndiwe mboni yeniyeni! Sizinapange kusiyana kulikonse, kuyesera kuzikopera izo, ndi kuyesera kuchita chinachake, kuchipanga icho kuwoneka monga icho; iye anagwira mokhazikika. Amatsengawo anabwerapo. “Mwaona,” Farao anati, “taonani, ndi matsenga enaake otchipa. Ndi Bezezebule, kuwerenga kwamalingaliro kwina kapena chinachake. Ine ndiri ndi amuna pano, amatsenga, akhoza kuchita chinthu chomwecho; am’bwebwe, kuti anyoze izo, chirichonse chimene icho chiri.” Izo sizinamuyimitse Mose. Iwo anali Mawu a Ambuye, chifukwa icho chinali chizindikiro cha Mwamalemba chikutsatira izo.

⁸⁹ “Oh, inde,” anati, “Bambo Kusakhulupirira, Bambo Kukayikira, ndi onsewo, analendewera pa mapewa anga. Koma ine ndinakhala molunjika kumene ndi Mawu amenewo, podziwa kuti Uyo anali Mulungu amene ananena Mawu, Ndi Mulungu woti awasamalire Iwo, osati iwowo. Iye anandiwuza ine kuti ndinali woti ndiwatengere ana amenewo ku dziko lolonjezedwa. Iye anandiua ine kuti ndinali woti ndiwatulutse iwo kumeneko, ndipo ndinali woti ndidzabwerere ku phiri ili kumene izo zinachitikira. Ine sindikudziwa kuti ndi motani. Farao anawopsyeza—anawopsyeza moyo wanga, ndipo chirichonse chinachitika, koma ndinakhale wokhulupirika ku lonjezolo. Potsiriza, Mulungu anamugonjetsa mdaniyo, ndipo ndinawawolotsa iwo pa Nyanja Yofiira, monga pa nthaka yowuma. Mulungu anasunga lonjezo Lake, ndipo ine ndinabwera molunjika ku phiri kumene Iye anandiua ine kuti ndikanadzabwerako, phiri lomwelo.” Mwaona, iye anali atakhulupirira kuti ameneyo anali Mulungu, ndipo iye anagwiritsitsa mokhazikika.

⁹⁰ Tiyeni tibweretse mboni ya nambala foro, pokhala kuti tikufulumira. Tiyeni tibweretse mboni ya nambala foro, Yoswa, amene analowa m’malo mwa Mose.

⁹¹ Yoswa anati, “Ine ndinapita kumeneko ndi azondiwo. Ine ndinatumizidwa uko. Thwelovu a ife tinatumizidwa; mmodzi kuchokera mu chipembedzo chirichonse.” Ndipo anati, “Ife tinapita kumusi uko ndipo ife tinakayang’ana. Ndipo apa iwo anabwerera, ali ndi mantha, ndipo anati, ‘Chabwino, ife tikuwoneka ngati ziwala, pambali pa anthu amenewo. Oh, mai, iwo ndi aakulu kuposa momwe ife tiriri! Iwo ndi anthu amphamvu, chimene iwo onse ali! Ife tikuwoneka ngati ziwala.’” Ndipo anati, “Pa Kadeshi-barnea ine ndinawakhazikitsa bata anthuwo, ndinati, ‘Yembekezani miniti. Inu mukuyang’ana pa chimphona ndi otsutsa. Ine ndikuyang’ana pa lonjezo la Mulungu. Mulungu anati, “Ine ndikupatsani inu dzikolo.”” Amen. Ine ndinawapangitsa anthuwo kukhala chete, chifukwa Mawu analonjeza zimenezo.

⁹² “Ndiye, tsiku ndi tsiku, iwo amabwera ndi kudzati, ‘Dzikolo liri kuti? Kodi mkakawo ndi uchi ziri kuti, Yoswa?

Iwe unalondejeza izo, nawenso. Kodi izo ziri kuti? ‘Mulungu adzasamalira izo.’ Ndipo Iye anawalola onse osakhulupirirawo kuti afe. Iye anandisunga ine wamoyo, anadzutsa kam’badwo kena. Patapita zaka forte, ife tinalitenga dzikolo. Mulungu ananena chomwecho!”

⁹³ Ndipo, kumbukirani, iwo anali pa ulendo wa masiku awiri okha. Iye anawabweza iwo mmbuyo kwa zaka forte chifukwa cha kusakhulupirira kwawo. Machiritso anu akhoza kusatalikira ndi maminiti faivi. Kusakhulupirira kwanu kukhoza kumawaika iwo patali ndi inu nthawiyonse inu muli moyo. Inu mukuyenera kukhulupirira izo! Iye ndi mboni yeniyeni, Yoswa. Inde, bwana. Iwo analitenga dzikolo, zaka forte mtsogolo.

⁹⁴ Ife tiri ndi mboni zambiri zimene tikanatha kuziyitana, koma, ngati mungandikhululukire ine, ine ndikufuna kuti ndikhale mboni Yake yotsatira. Ndikufuna kudzipereka ndekha ngati mboni Yake, ngati sizimveka mwaumwini kwambiri. Ine ndi mboni Yake. Ine ndikufuna kuti ndikhale Yake yotsatira, mboni Yake yachisanu.

⁹⁵ Mulungu angakhoze bwanji kutenga chisoso ndi kupanga njere ya tirigu kuchokera mwa icho? Wochimwa, wochokera ku banja lochimwa; onse a iwo ali ndi mifuti, ndipo amafa atavala nsapato zawo; oledzera ndi zina zimene inu muli nazo. Bwanji, ine ndinalibe kanthu kochita ndi izo.

⁹⁶ Amayi anga amene ali mu Ulemelero lero, anati, ora limene ine ndinabadwa, Mngelo wa Ambuye uja analowera pa zenera ndipo anadzayima pamwamba pa chikuta chimene ine ndinalimo. Iwo ali ndi chithunzi cha Iye mu maholo asayansi a Luso la Chipembedzo lero. Izo nzodziwika padziko lonse lapansi. Mulungu analondejeza kuti akanadzachita zinthu zimenezi. Monga mnyamata wamng’ono, Liwu linayankhula kwa ine, linati, “Usadzasute konse, kutafuna, kapena kumwa, kuyipitsa thupi lako mwanjira iliyonse. Padzakhala ntchito yoti iwe udzagwire ukadzakula.” Zinandichititsa mantha, ndithudi.

⁹⁷ Kodi ine ndinkadziwa chiyani za chipembedzo? Anthu anga, poyamba, anali Akatolika. Kodi ine ndinadziwa bwanji chirichonse chokhudza zinthu zimenezi? Sindinakhalepo mu tchalitchi m’moyo mwanga. Iwo onse anakwatirana kunja kwa mpingo, kotero iwo basi. . . . Amayi ndi abambo, awiri onse, anali achi Airishi, ndipo kotero iwo anangokwatirana kunja kwa tchalitchi, ndipo ife tinalibe chipembedzo.

⁹⁸ Ife tinkangokhala ngati gulu la agalu, tinali ndi kanyumba komakasamutsa kakale, ngati okhala mu msasa, kuchoka pamalo kupita pamalo, kulikonse kumene tingapeze kachisakasa kakang’ono tinkakhoza kulipira lendi ya madola atatu kapena anayi pamwezi. Umo ndi momwe ife tinkakhalira.

⁹⁹ Mnyamata wamng’ono wopanda nsapato, atanyamula madzi kukapangira kachasu, tsiku lina; pamene Mulungu,

mukuchita kwayekha Kwake, akusungabe Mawu Ake, anatsika mu kamvuluvulu ndipo anayima pamenepo, ndipo anati, “Iwe usamachite zinthu izi.” Iye ananena zimenezo. Pamene ine ndinadzakhala mnyamata wamng’ono, masomphenya anayamba kuwonekera mmaso mwanga, kuchokera kwa mnyamata wamng’ono kwambiri. Izo zinandiwopsya ine. Ine ndinapulumsidwa, ndipo ine ndinalowa mpingo wa Baptisti. Ine ndinafunsa. . .

¹⁰⁰ Ine ndinawauza abale anga Achibaptisti za kupita... Sindinkadziwa kuti ndizitche izo chiyani, masomphenya. Ndinazitcha izo chizimbwizimbwi. Ndipo ine ndinapita ndi kukawauza abale anga za izo. Iwo anati, “Billy, usakhale ndi chochita ndi zimenezo. Ameneyo ndi mdierekezi. Ameneyo ndi mdierekezi. Iwe usakhale ndi chochita ndi zimenezo.”

¹⁰¹ Usiku wina, ku msasa wawung’ono kumene ine ndinkawedza, kutali komwe mmapiri, ine ndinali nditagona kumbuyo uko. Pafupifupi firii koloko mmawa wina, ine ndinawona Kuwala kukubwera. Ine ndinali ndikungowerenga Baibulo. Ine ndinaganiza kuti anali winawake akubwera, akuwunika kudzera pa bowo la mtengo, nyali kapena chinachake. Uko kunali kutali mnkhalango. Ndipo ine ndinaganiza kuti winawake anali akubwera. Kuwalako kunali pans; Iko kunafalikira mokulirapo ndi mokulirapo. Ine ndinamumva Winawake akuyenda. Pamene Izo zinatero, Uyo anali Munthu. Iye anali wopanda nsapato. Iye anali ndi tsitsi lofika mmapewa Ake, ndipo Iye anali atavala mkanjo. Ndipo zinakhala ngati zandiwopsyeza ine pafupi kufa.

¹⁰² Iye anati, “Usachite mantha. Ine ndatumidwa kuchokera mu Kukhalapo kwa Ambuye Mulungu, kudzakuuza iwe kuti moyo wako wosamvetsetseka, usayesere kuchoka ku zinthu izi, amenewo ndi mayitanidwe ako. Ndipo Mulungu adzakhala akukutumiza iwe ku malo osiyanasiyana ku dziko lonse, kuti ukapempherere odwala. Ndipo ngati iwe udzawapangitse anthu kuti akhulupirire ndi kukhala owonamtima, palibe chimene chidzayime patsogolo pa pemphero.”

¹⁰³ Izo zinandiwopsya pafupi kufa. Ndithudi, izo zinatero. Ine ndinayima pamenepo, ndipo—ndipo Iye anapitiriza kuyankhula. Ine ndinati, “Bwana, ine ndiri kuno chifukwa cha zizimbwizimbwi zimenezo ndi zinthu monga izo.”

¹⁰⁴ Iye anati, “Padzakhala zinthu zitatu zimene zidzachitike. Choyamba, iwe udzadziwa potenga dzanja lako ndi kuwagwira anthu. Kenako izo zidzafika pochitika, zikadzatha zimenezo, ngati iwe uti udzakhale owonamtima, kuti iwe uzidzadziwa chinsinsi chomwe chiri mu mtima mwawo.”

¹⁰⁵ Ndipo ine ndinati, “Icho ndi chimene ine ndabwerera kuno kuti ndidzayankhule, ndinali ine. . . Abale anga anandiwuza ine

kuti izo zinali za mdierekezi. Ine ndi Mkhristu. Ine sindikufuna kukhala chirichonse cha mdierekezi.”

¹⁰⁶ Iye anati, “Monga izo zinali kumbuyo uko, chomwechonso izo ziri tsopano. Pamene iwo ankakangana za mtundu wa mabatani omwe iwo amayenera kuyika pa zikhotho zawo, ndi zinthu monga izo, ndipo atumiki akunena kuti Paulo ndi iwo anatembenuza dziko pansi, icho chinali chiyani? Koma unali a—mzimu woyipa umene unati, ‘Amuna awa ndi atumiki a Mulungu, amene akutembenuza dziko lapansi chadodolido,’ Paulo ndi iwo.” Anati, “Mzimu woyipawo unachitira umboni kuti iwo anali atumiki enieni a Mulungu.”

¹⁰⁷ Iye anandiuza ine, anati, “Kodi iwe sukukumbukira, Mmalemba, icho ndi chinthu chimene Ambuye wathu anachita? Ndipo icho ndi chimene Iye analonjeza, Iye anati izo zikanadzachitika kenanso mmasiku otsiriza.”

Ndinaganiza, “Chabwino, kodi chimenecho chingakhale chiyani?”

¹⁰⁸ Iye anati, “Chabwino, iwo ndi Mzimu wa Ambuye Yesu. Iye ndi Mawu. Ndipo Iye analonjeza izi mmasiku otsiriza. Tsopano usachite mantha.”

¹⁰⁹ Ine ndinapita kumusi kuti ndikabatize gulu la anthu pa mtsinje. Pamene ine ndinkabatiza kumeneko, kumene pafupifupi anthu faivi sauzande anali atayima pa gombe, pakati pa tsiku penipeni, thuu koloko masana, kukutentha, iwo anali asanakhale ndi mvula kwa sabata kapena awiri, ndipo atayima pa gombe, apo panabwera Lawi la Moto lija likuzungulira kuchokera mu mlengalenga, likubwera pansi pamene ine ndinali nditayima, ndipo Liwu likuti, “Monga Yohane M’batizi anatumidwa, ndi kudzatsogolera kudza koyamba kwa Khristu, Uthenga wako udzatsogolera Kudza Kwachiwiri kwa Khristu.”

¹¹⁰ Nyuzipepala zinazilemba izo, ndipo zinasesa mpaka ku Canada pa Associated Press, kuzungulira dziko lapansi, “Mtumiki wamba, mtumiki wa Baptisti, akubatiza, ndipo,” anati, “Kuvala kwachinsinsi kunawonekera pa iye.” Mmodzi yemweyo amene iwo anamujambula chithunzi chake kuno, ndipo anachita icho mu Germany ndi—ndi kulikonse. Ndipo izo zachitidwa.

¹¹¹ M’busa wanga anati kwa ine, iye anati, “Billy, ndi loto lotani limene iwe unali nalo? Bwanji, iwe ukudziwa kuti sunawone . . .”

Ine ndinati, “Panali mahandirede atayima pamenepo, amawona Izo.”

¹¹² Ndipo iwo ankakhoza kubwera, nkumati, “Oh, uko ndi kubalalika kwa ubongo.” Akuyesetsa momwe angathere, ameneyo ndi bambo wachikulire Kusakhulupirira ndi Bambo Kukayikira.

113 Ine ndinagwiritsitsa molunjika ku Mawu. Ndinakhala pamenepo, chifukwa ine ndinkadziwa kuti ilo linali lonjezo la Mulungu. Amen. Luka mutu wa 17, Iye analonjeza, “Monga zinali mmasiku a Sodomu.” Pamene ine ndinawona dziko likuwunjikana, monga izo zimachitikira, ine ndinadziwa kuti chinachake chikuyenera kukwaniritsidwa. Ine ndinawona mu Malaki 4, pamene iwo akanati “adzabwezeretse Chikhulupiriro ku Mawu,” chimene iwo anali atabalalika kuchokako. Ine ndinadziwa kuti izo zinkayenera kuchitika, ndipo ine ndinakhala woona ku Mawu. Ine ndikumupeza Yesu Khristu, lero, “yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

Osonkhana, kukugwa mvula. Ine ndiyimira pomwepa.

114 Ine ndikufuna kunena ichi. Ine ndabweretsa mboni zonsezi; umboni wanga womwe. Ambiri a inu ndi mboni, sabata yino. Chinthu chimenecho ndi choona, Uthenga. Ine ndingathe bwanji...

115 Dokotala Davis anati kwa ine, “Mnyamata, wamaphunziro a sukulu ya galamala, kupita kukapempherera mafumu ndi olamulira, ndi kukayatsa chitsitsimutso chimene chidzazungulire padziko lonse lapansi? Billy, tayamba wazidekhetsa kaye wekha.”

116 Koma, Iwo unachita izo! Iwo unachita izo! Zaka sarte-firii zitatha, chitsitsimutso chinafalikira, ndipo Iwo unachita izo. Mulungu ananena chomwecho! Ine ndine mboni Yake. Iye sananene kuti *liti* limene Iye akanati adzachite izo. Iye anati Iye akanadzachita izo! Ine ndinayembekezera nthawi imene Mawu akanadzakhala enieni kwambiri, atayikidwa mdzanja langa, monga linachitira, Lupanga, ndipo akanadzakhocha kumazindikira malingaliro omwe a mu mtima mwa anthu. Ine ndinaganiza, “Izo zingakhale motani?” Ine ndinadikirira, ndikukhulupirira izo, ndipo izo zinadzachitika. Wonyoza, Wosakhulupirira, Wokayikira, Wosapirira, akudikirirabe ndipo akuyang’anabe. Koma Mulungu, zitatha zaka sarte-firii, wazitsimikizira izo, kulikonse, kuzungulira dziko lapansi. Kumene mapepala, magazini ndi nkhani zalembedwa, kuzungulira dziko lonse lapansi.

117 Inu mukhale oweruza. Malingaliro anu ndi ogamula. Ogamula aliyense akuyenera kupanga lingaliro lake. Ine ndikutseka khoti. Inu mukhale oweruza. Malingaliro anu ndi ogamula. Ndipo zochita zanu kuchokera pano, masana ano, pamene ife tiziyika manja pa odwala, izo zifotokoza chimene chigamulo chanu chinali. Momwe inu mutachitire mukatha kupemphereredwa, izo zifotokoza chimene malingaliro anu aluntha apanga, chimene wogamula wa malingaliro anu wapanga. Izo zifotokoza ndendende basi, zochita zanu kuchokera pano.

118 Ine ndikulengeza kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndikulengeza kuti palibe kanthu kangakhoze kuyima mu Kukhalapo Kwake, kwa amuna ndi akazi amene ati akhulupirire izo. Kodi inu mukukhulupirira izo?

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

119 Ambuye, Yesu, mawu okha ochokera kwa Inu tsopano, apangitseni anthu kukhulupirira. Iwo akhala pano. Ine sindikanati ndichite izi, Atate. Koma, iwo akhala opirira kwambiri, ine ndikupempha tsopano. Kodi Inu simutero, pa umboni wanga womwe?

120 Ife tikhoza kuwerenga mu Baibulo, mboni za anthu amenewo, mboni ya osakhulupirira. Ife tikuwona pamene iwo nthawizonse akhala akuzitsutsa Izo. Afarisi amenewo, anthu achipembedzo mmasiku amenewo, ankamutsutsa Yesu Khristu. Koma izo zinatsimikizira, Iye anali Mwana wa Mulungu. Iwo anati, “Iwe ukudzipanga Wekha kukhala Mulungu.” Iye anali Mulungu. Iye ankachita ngati Mulungu; Iye ank'alalikira ngati Mulungu; Iye ankachiza ngati Mulungu; Iye anawuka kwa akufa ngati Mulungu; Iye anakwera Mmwamba ngati Mulungu. Iye ndi Mulungu. Iye akubwera, Mulungu. Ife tikuzikhulupirira zimenezo. Mkatikati mwa zovuta zonse, Inu mukadali Mulungu. Umboni Wanu ukuyima, Ambuye.

121 Ine ndikuchitira izo umboni, kapena ndinayankhula za maumboni a anthu ena awa. Masauzande kuchulukitsa masauzande ine ndikanakhoza kuwaitana, kumbali ziwiri zonse; wokayikira, wosakhulupirira, ndi munthu amene sangakhoze kudikira utali wokwanira. Inu simunanene kuti *liti*. Inu munati, “Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, ngati iwo akhulupirira, iwo adzachiritsidwa, ziribe kanthu kuti ndi nthawi yanji. Inu simunamuuze konse Abrahamu kuti mwanayo adzabadwa liti. Inu simunamuuze Mose tsiku limene iye akanati adzawabweretse anthuwo kubwerera ku phiri limenelo. Inu simunamuuze Nowa tsiku limene mvula ikanati idzavumbe. Inu simunawauze iwo nthawi ina iliyonse; ngakhalenso Inu simunatiwuze ife.

122 Inu munati, “Ngati inu mungakhulupirire! Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, osakayikira mu mtima mwanu, izo zidzachitika, chimene inu mwachiyankhula. Ngati mukhulupirira izo!” Inu munati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Ambuye, ndaziyanenso izo pa miyendo pa anthu. Izo ziri kwa iwo.

123 Ine ndatsimikizira kwa iwo, ndi Baibulo, ndipo ife tonse tikudziwa izo, kuti Chitetezero chinapangidwa. “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu. Ndi mikwingwirima Yake ife *tinachiritsidwa*.” Ndi nthawi yakale, kuti atseke pakamwa pa wokayikira, ndi wosakhulupirira amene anati Iye

sanawuke, ndi kuyesetsa kupanga izo mtundu wina wa Mulungu wa mbiriyakale mu chipembedzo.

¹²⁴ Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mumuwonekeretse Iye kachiwiri masana ano pakati pathu, ndipo mutsimikizire kwa omvetsera awa kuti Inu muli pano; Mmodzi amene ananena Mawuwo, Mulungu amene ife takhala naye pa mlandu. Kwa ine, Inu mwalungamitsidwa, Ambuye Mulungu. Inu mwazitsimikizira Nokha, Mulungu. Dzipangeni Nokha kukhala weniweni kwambiri, kuti mwamuna ndi mkazi aliyense, anthu osauka awa amene akhala pano mu khola lodontha ili pano, akuyesetsa kuti amve Mawu, apangeni Iwo kukhala enieni kwambiri kwa iwo, Atate. Dziwonetsereni Nokha kuti ndinu Mulungu pakati pathu!

¹²⁵ Momwe anthu mmibadwo yonse, Izo zabwera ngati zachirendo, kwa anthu. Pamene iwo anali pa nyanja usiku umenewo, ndipo—ndipo Inu munadza kwa iwo, iwo ankaganiza kuti uwo unali mzimu. Iwo anali. . . Iwo sankadziwa chimene icho chinali, ndipo iwo anafuula. Koma Liwu lija linabwereranso, “Ndi Ine.”

¹²⁶ Liwu la Lemba likunena, masana ano, kuti lino ndi oralo, ino ndi nthawiyo, Sodomu ndi Gomora ndi zinthu zina zonsezi zikukhala momwe izo zimayenera kukhalira. Ndipo apa Inu muli, mukuwonetsera kwa Mbewu yachifumu ya Abrahamu kuti Inu muli moyo, ndipo Mwana wa munthu akuwululidwa mu tsiku lino la Sodomu. Atate a Kumwamba, lolani kuti anthu awone; ndipo, pamene iwo azibwera, kuti iwo atenge Mawu a Mulungu basi monga momwe Abrahamu anachitira. Ziribe kanthu kuti mwanayo. . .

¹²⁷ Ife tikanatha kumuyitanira Yesaya pa chochitika, ndipo Yesaya akanatha kuchitira umboni. Iye akanati, “Ambuye anati kwa ine, ‘Namwali adzayima.’” Ngati iye akanawuka ndi kudzayankhula nafe masana ano, mosakayika koma chimene iye akanati anene, “Mtsikana wamng’ono aliyense Wachihebri, kudutsa mmasiku anga onse, ankayembekezera kuti atenge pakati pa Mzimu Woyera; aliyense. Koma Inu munanena izo, munazilemba izo. Inu munandizindikiritsa ine ngati mneneri Wanu. Ndipo mawu anga amene ine ndinkanena anayimikiridwa kumbuyo ndi Inu. Masomphenya anga anali owona. Ndipo anthu anakhulupirira izo, kwa m’badwo kapena iwiri, ndiyeno izo zinazimirira. Komabe, patapita zaka eyiti handiredede, namwali anakhala ndi pakati ndipo mwana anabadwa. Dzina Lake linali ‘Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, ndi Atate Wosatha,’ zaka eyiti handiredede mtsogolo.”

¹²⁸ O Ambuye Mulungu, chavuta ndi chiyani ndi anthu awa, za ife pa dziko lapansi lino lero, kuti tizidzitcha tokha Mbewu yachifumu ya Abrahamu? Pamene, iye anadikirira zaka twente-faivi, akuyembekezera ndi—ndi kukhala ndi

chikhulupiriro chotsutsana ndi zosatheka, kuti awone chozizwitsa chikuchitidwa, ndipo Inu munachita icho. Ndi mochuluka bwanji momwe ife tingatengere Mawu Anu, pamene Inu muli Mulungu wowoneka yemweyo amene anawonekera kwa Abrahamu, amene akuwonekera pano kwa ife mu thupi laumunthu, mwanjira yomweyo imene Inu munachitira kwa Abrahamu! Mulungu, perekani kuti iwo atero, aliyense, awone izo masana ano, ndi kuchita bwino. Nthawi iriyonse pamene anthu azidutsa, ndipo manja akayikidwa pa iwo, mulole kuti iwo apite kuchokera mchipinda chino, akusangalala, ndipo osachichotsa konse icho, koma akhulupirire monga Abrahamu ndi mbadwa zina zonse. Inu munati izo zikanadzachitika, ndipo zidzachitika ngati iwo satopa. Perekani izi, mu Dzina la Yesu. Amen.

¹²⁹ Ine ndikukhulupirira. Ine ndikukhulupirira. Inu mukhulupirire! Ine ndimakhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu. Ine ndimakhulupirira kuti Iye anawuka kwa akufa. Ine ndikukhulupirira kuti Iye ali wokhoza koposa kuchita lonjezo lililonse limene Iye analonjeza kuti akanadzachita. Iye akhoza kusunga mawu aliwonse amene Iye anayamba wanenapo, ndipo Iye atichitira ife pano masana ano ngati ife titangokhulupirira izo.

¹³⁰ Tsopano, Iye sanati, “Pitani inu tsopano, ndi—ndipo mukawagwedeze anthu mzikuku, ndi kukatenga mavuto a mtima ndi kukachita *ichi*.” Iye sananene zimenezo.

¹³¹ Anati, “Kayikeni manja pa odwala, ndipo iwo adzachira.” Amenewo ndi okhulupirira.

¹³² Tsopano, Mzimu Woyera ndi mboni Yake pano, Iye akudziwa ngati inu mukukhulupirira Izo kapena ayi. Musangobwera, mukungopenekera. Mutenge kupenekera kumeneko, ndipo mutenge chiyembekezo chimenecho, ndi kutenga cholingalira chimenecho, ndipo muziyike izo pansi pa mapazi anu, ndipo munene kuti, “Ine ndiri ndi chikhulupiriro, ndikudziwa kuti izo zitero!” Chinachake chichitika.

¹³³ Kodi inu mukuganiza kuti icho ndi chiyani, kwa ine, nditayima apa, amzanga? Inu mukuganiza chiyani, kwa ine, nditayima pano monga ziriri tsopano, pamaso pa omvetsera nthawizina mpaka masauzande, ndi mahandiredede a masauzande, nkumanena kuti Iye ndi wamoyo, ndipo Mzimu Wake unandiiza ine kuti Mawu amene Iye akanandipatsa ine...? Kodi Mulungu angachite chirichonse popanda kuchiyimirira icho kumbuyo? Mwaona, ananena kuti Iye akanadzachita izo! Amenewo ndi Mawu. Ndi kuyima pano pamaso pa omvetsera, pamene okayikira, osakhulupirira, ndi china chirichonse chitakhala, mwa mateni amasauzande; ndipo komabe nkumuwona Iye, kumuyitanira Iye pa chochitika.

¹³⁴ Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali pano? Chabwino.

¹³⁵ Winawake amene ali pafupi. Osati azimzanga tsopano; ngati inu muli—ngati inu mukudwala, aliyense, azimzanga. Ndi angati, pomwe pano patsogolo panga, mukudziwa kuti ine sindikukudziwani inu, kwezani mmwamba manja anu monga *chonchi*?...?...

¹³⁶ Tsopano alipo ena muno amene amandidziwa ine. Mwaona, cha *apa*, iwo akundidziwa ine, pomwe pano. Uko nkulondola, sichoncho izo, abale, nonsenu cha pamenepo? Mukuona? Yang'anani apa. Mwaona, iwo amandidziwa ine.

Koma kunja *kuno*, inu simukundidziwa ine.

¹³⁷ Ndi angati mu mzere umodzi uwu pano amene samandidziwa ine, kwezani anu... Kodi pali aliyense m'mizere itatu iyi apa, momwe *muno*, amene amandidziwa ine; akudziwa kuti ine ndikudziwa chinachake cha inu, ndi chirichonse? Kwezani mmwamba manja anu.

¹³⁸ Kodi ine ndikukudziwani *inu* kumbuyo uko? Ndikukudziwani *inu*, m'bale? Ine sindikukhulupirira kuti iye anandimvetsa ine, chifukwa ine sindikumudziwa iye. Iye sakundidziwa ine. Ayi. Inu simukundidziwa ine, sichoncho inu, bwana? Inu—inu—inu mukundidziwa ine? Kodi mukudziwa kuti ine ndikudziwa chimene chalakwika ndi inu? Inu ndi ndani? Mwinamwake iye sakundimvetsa ine; chifukwa ine—ine sindikumudziwa mwamunayo. Tsopano inu munatani... Kodi inu mukudziwa kuti ine ndikudziwa chimene chiri cholakwika ndi inu; popanda kukhala wauzimu, Ine ndikungokudziwani inu ngati munthu, ndipo ndingadziwe chimene chiri cholakwika ndi inu? [M'baleyo akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Ndithudi ayi. Ndithudi. Mwaona, ine sindingatero. Mwaona, kukugwa mvula, ndipo inu simungamve.

¹³⁹ Mzimu Woyera utithandize ife tsopano. Chabwino, kuyambira gawo *ili* ndiye. Inu mukhulupirire, mkati *muno*.

¹⁴⁰ Munthu mmodzi ameneyo, tsopano, iye ine—ine mwinamwake sindingakhoze kudziwa nkomwe. Mwamuna wakhala apo, iye wakweza dzanja lake mmwamba, mwaona, ine sindikuganiza... Iye samandidziwa ine. Ndikudziwa kuti iye samatero. Koma iye wangoyika... anakweza dzanja lake mmwamba, mulimonse. Ine sindimukhudza iye, ndiye, mwaona. Ine...

¹⁴¹ Mukhale *inu* nonse... Ambuye akudalitseni. Winawake akupemphera, mkati *muno*. Kodi inu mukukhulupirira? Aliyense wa inu, kodi inu mukumukhulupirira Iye? Ndi mtima wanu wonse, khulupirirani.

¹⁴² Apa pali dona wamng'ono. Ndiroleni ine ndingoyitana munthu mmodzi, ndiyambe kuyankhula, ndingoyankhula kwa winawake; kutenga Wake... kuyambitsa Mzimu Woyera kuti uzisuntha. Dona wamng'ono wakhala apo, kodi iwe ukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu?

Iwe, dona wamng'ono wakhala pomwe apa. Mukuona? Inu, chabwino, awiri a inu munagwedeza mitu yanu. Chabwino, tingokhala ndi nonse awiri ndiye. Chabwino.

¹⁴³ Dona apa, unagwedeza mutu wako monga *chonchi*; wavala diresi la pinki. Ngati Yesu Khristu angandiwuze ine lomwe liri vuto lako, kapena chinachake chokhudza iwe, kodi iwe undikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake; kudziwa kuti ndi Iye? Vuto lako liri kunsana kwako. Ngati izo ziri zoona, kweza mmwamba dzanja lako. Mukuona? Mukuona? Mukuona? Chabwino. Mukuona? Mukuona?

¹⁴⁴ Tsopano, iwe, dona wamng'ono uko kumapeto, iwe sunamve izo chifukwa nyengo inali yoyipa. Iwe uli ndi vuto la thumbo. Kapena mtima. . . Vuto la thumbo, liri mu thumbo lako.

Mkazi uyu wakhala pafupi ndi iwe, ali ndi vuto la mtima.

¹⁴⁵ Ngati izo ziri zoona, inu akazi atatu kwezani mmwamba manja anu. Ndipo ndine mlendo kwa inu, mwaona.

Tsopano kodi inu mukukhulupirira? Khalani ndi chikhulupiriro. Ndizo zonse zimene inu mukuyenera kuchita.

¹⁴⁶ Dona wamng'ono wakhala pomwe pano, akuyang'ana pa ine pomwe, ine sindikukudziwa iwe. Ndiwe mlendo kwa ine. Iwe su—sukundidziwa ine. Wakhala pomwe apo, ndi yoyera pang'ono. . . ukuyang'ana pa ine pomwe. Inde, iwe. Uh-huh. Iwe sumandidziwa ine. Koma iwe ukuvutika, sichoncho iwe? Iwe umakhala ngati umadandaula pang'ono za chinachake. Ndi chotupa chimene chiri mu bere lako. Ngati izo ziri zoona, kweza mmwamba dzanja lako.

Tsopano, iwe ukuti, “Inu mwawona chotupa.” Palibe chotupa chimene chikuwonekera.

¹⁴⁷ Nkulondola uko? Palibe chotupa chimene chikuwonekera. Ndipo ine sindikukudziwa iwe. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiiza ine yemwe iwe uli? Kodi izo zikuthandiza iwe mwanjira ina? Kodi izi zingathandize omvetsera? Tsopano, kumbukirani, mkaziyo wakweza dzanja lake mmwamba. Kweza dzanja lako mmwamba, ine sindikukudziwa iwe. Mulungu andithandize. Akazi a Patterson. Uko nkulondola. Kodi ukukhulupirira?

¹⁴⁸ Tiri pomwepo, awo ndi apongozi ako akhala pafupi ndi iwe apo. Kodi inu mukukhulupirira? Iwo akufuna kuti apemphereredwe. Iwo abwerera cholinga chimenecho. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiiza ine lomwe liri vuto ndi iwo? Vuto lawo liri m'maso mwawo ndi m'makutu mwawo. Ngati izo ziri zoona, kweza mmwamba dzanja lako. Uko nkulondola.

Iye ali moyo! Iye akadali Mulungu.

¹⁴⁹ Apa pali dona wakhala kumbuyo uko, ali ndi khunyu. Iye ali ndi khunyu, ndipo iye ali ndi vuto lachikazi. Ndipo dzina lake

ndi Abiti Woods. Ngati izo ziri zowona, imirira pa mapazi ako. Imirira pa mapazi ako ngati izo ziri zowona. Ine sindinayambe ndamuwonapo mkaziyo mmoyo wanga. Mdierekezi wakusiya iwe pamenepo, mlongo. Matamando akhale kwa Mulungu! “Ngati inu mungakhulupirire.” Inu mungokhulupirira.

¹⁵⁰ Apa pali dona wakhala kumbuyo komwe *kuno*. Iye ndi wofooka kwambiri. Iye akudwala. Iye wangobwera kuchokera ku chipatala. Iye ali ndi—ali ndi vuto la m’imba. Dzina lake ndi Abiti Kitchens. Imirira, ndipo ukhulupirire ndi mtima wako wonse, Yesu Khristu wakuchiza iwe. Sindinamuwonepo iye m’moyo wanga.

¹⁵¹ Apa pali dona amene ali ndi vuto la ndulu. Kodi iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse, nawenso, kuti Mulungu akuchiza iwe? Akazi a Whittaker, kodi iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse, Mulungu akuchiritsa iwe? Ngati izo ziri zoon, imirira pa mapazi ako, ngati ife tiri alendo kwa wina ndi mzake.

¹⁵² Kodi iwe ukukhulupirira kuti Iye ali pano? Chimenecho ndi chiyani? Imeneyo ndi mboni ya woyimbidwa mlandu ya Mulungu. Aleluya! O anthu, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse! Imeneyo ndi mboni ya woyimbidwa mlandu ya Mulungu.

¹⁵³ Inu mukumuweruza motani Iye? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akulondola? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mawu Ake ndi owona? Iye analonjeza! Sabata yonseyi, ine ndalalikira pa izo ndi kuwonetsera izo mu Baibulo, kuti Iye akanadzachita izi mu tsiku lino. Kodi inu mukukhulupirira kuti icho ndi Choonadi? Kodi inu mukuweruza? Kuweruza kwanu ndi kotani? Kodi inu mukukhulupirira?

¹⁵⁴ Aloleni iwo amene ali ndi makadi apemphero mbali iyi cha *apa*, ayimirire pakati pa kanjirako, cha *kuno*, amene ali ndi makadi apemphero, pa mzere uwu cha *apa*; imirirani pakati pa kanjirako, njira iyi. Iwo ali mbali *iyi*, amene ali ndi makadi apemphero, imirirani mu kanjira *ako*, njira iyi. Iwo ali mbali inayo, imirirani mu kanjira *ako*.

¹⁵⁵ Iwo amene ali mmwamba umo, amene ali ndi makadi apemphero, yendani mukutsikira kutsogolo.

¹⁵⁶ Iwo amene ali mu mzere *uwu* apa, amene ali ndi makadi apemphero, imani cha mbali *imeneyo*. Iwo amene ali mbali *iyi* ali ndi makadi apemphero, imirirani mu kanjira *aka* pomwe pano. Iwo amene ali ndi makadi apemphero, *apa*, imani mu kanjira *aka*.

¹⁵⁷ Tsopano, imani pamenepo tsopano. Ife titenga mbali inayo mu miniti yokha. Pangani mzere wanu. Bwerani pansu pomwe. Ine ndi . . .

¹⁵⁸ Tsopano dikirani, miniti yokha, pamene inu mulipo. Imani pomwe inu mulipo, mphindi yokha.

¹⁵⁹ Penyani, ndi atumiki angati ali muno, amene akukhulupirira, munthu weniweni wowopa Mulungu amene akukhulupirira kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, kuti kutuma Kwake kotsiriza kwa Mpingo Wake, kunali, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira; ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira”? Ndi angati a inu atumiki mukukhulupirira zimenezo? Ngati inu mukutero, bwerani kuno ndi kudzayima ndi ine pomwe pano pamene ife tikupemphera. Kuchitira kuti pamene anthu awa akuchiritsidwa, iwo awone kuti sanali M’bale Branham yekha; ndi inu, aponso. Imani motsatira *apa*, pangani mizere iwiri pomwe *apa* pamene mzerewo utadutse. Oh, mai! Kodi Mulungu angachitenso chiyani? Ine sindikudziwa kalikonse. Yang’anani pa atumiki amene akubwera kudzachitira umboni za izi. Pitani mmusi momwe, pangani mzere wanu pansi njira *iyi* apa.

¹⁶⁰ Huh? [Winawake akuti kwa M’bale Branham, “Sindingathe kuwapangitsa iwo kuti asunthe.”—Mkonzi]. Huh? [“Sindingathe kuwapangitsa iwo kuti asunthire pansi apa.”] Izo ziri bwino. Izo ziri bwino. Ife tiwapeza iwo.

¹⁶¹ Tsopano ine ndimuyitana M’bale Borders, manenjala, kuti abwere kuno pa mayikrofoni iyi. Ndipo ine ndikufuna kuti asunge mzerewo mu dongosolo, kuchitira kuti iwo azidzera njira *iyi*, nkumabwerera mmbuyo njira *iyi*, ndi kumabwerera ku mpando wanu, mwaona, pamene inu muzibwera.

Tsopano nonse amene mukundimva ine, kwezani mmwamba dzanja lanu.

¹⁶² Taonani, mulole *awa*, ali kutali kwambiri kumbuyoko, abwere poyamba; ndipo abwere mozungulira mbali iyi, ndi kupita mozungulira. Kenako mulole otsatira. Azipita mozungulira kuseri kwa atumikiwa apa, pamene inu mwapemphereredwa, muzibwerera mmbuyo ndi kukakhala pa mpando wanu. Ndiye mulole Billy, iye azikupatsani chizindikiro mozungulira ndi kukuuzani inu momwe mungalowere mu mzere. Ndiyenso mwamsanga izi zikangotha, ife tiwalola iwo kuti ayime mmusi njira *iyi*, ndi kumadzera njira yina iyi.

¹⁶³ Tsopano nonse, amene mukumvetsa, kwezani mmwamba dzanja lanu tsopano. Chabwino, ziribwino. Tsopano M’bale Borders akhala pomwe pano pa mayikrofoni, kumachitira umboni pa zimene inu mukuyenera kuchita. Chabwino.

¹⁶⁴ Tsopano yang’anani. Chifukwa chimene ine ndikuchitira izi, ndi chifukwa chakuti ine ndikufuna kuti mumvetse. Ine sindikuwadziwa abale awa pano. Ine ndikuwadziwa awiri kapena atatu a iwo. Iwo akhoza kukhala Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria. Sindikudziwa kuti iwo ndi ndani. Palibe chifukwa choti ndinenere zimenezo. Mukuona? Tsopano, ine ndikufuna kuti inu mudziwe kuti ine ndikapita . . .

¹⁶⁵ Nthawi zambiri, mvangeri amabwera mtawuni ndipo iye amachita chirichonse, mwaona, iye amapempherera odwala ndi chirichonse. Mwaona, izo sizolondola. Ine ndikufuna kuti ndisakhale pa chithunzi chimenecho.

¹⁶⁶ Ine ndikufuna kuti inu mumuwone Yesu. Sabata ino, ndayetsa mwakuthekera kwanga kukuwonetsani inu kuti Iye ali pano. Ndipo ngati inu muli ndi chikhulupiriro, mungofikira mmwamba ndi kumupeza Iye, simukusowa kubwera mu mzere. Koma ngati inu mukufuna kutsatira Lemba ili, Kupezeka Kwake Kwauzimu, inu mwakhudza chovala Chake. Tangoyang'anani, chimene, anthu awa amene anayima pano, kanthawi kapitako, Mulungu Kumwamba akudziwa kuti ine sindinawawonepo iwo mmoyo mwanga. Ndipo ine ndikanakhoza kuyambira pomwe pano, mu maminiti pang'ono ine ndikhoza kukomoka. Ndi angati amene akudziwa kuti Yesu, pamene izo zinachitika kwa Iye, mkazi uja akugwiritsa ntchito mphatso ya Mulungu, iye anafooka? Ndi angati akudziwa kuti ukoma unatuluka mwa Iye, inali mphamvu Yake? Ndipo ndine wochimwa. Koma Yesu anati, "Zoposa izi inu mudzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga."

¹⁶⁷ Tsopano ife tipereka pemphero. Ndipo ine ndikufuna atumiki awa ndi ine. Ine ndiyima pomwe apa, nanenso, kuyika manja pa wodwala aliyense. Ndipo tsopano ngati inu. . .

¹⁶⁸ Kumbukirani! Mvetserani! Mvetserani inu kwa Iwo! Khulupirirani izo! Pokhapokha inu mutadutsa, mukukhulupirira kuti, "Pakali pano zakonzedwa mpaka kalekale," musabwere. Izo zingokupangitsani inu kuyipitsitsa. Izo zilepheretsa chikhulupiriro chanu. Koma ngati inu mukukhulupirira kuti muli mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, ndipo osati ife antchito Ake. Ndipo ife tikungochitira, maumboni, pamene ife tikuyika manja athu pa inu, kuti ife tikukhulupirira kuti ichi ndi Choonadi. Ndipo pamene ife tikuyika manja pa inu, inu mukhulupirire izo ndipo mutuluke muno, mukusangalala, mukuti, "Zikomo Inu, Ambuye! Zonse zakonzedwa." Musasinthe konse malingaliro anu.

¹⁶⁹ Tsopano kumbukirani. Ndiroleni ine ndibwerezenso izi. Mvetserani mwacheru. Malingaliro anu ndi ogamula wanu, pa mlandu uwu. Ndipo zochita zanu kuchokera pano, zidzakhala, zidzanena chimene chiweruzo chanu chiri. Inu munabwera kuno ndikuti, "Chabwino, ine sindikudziwa," inu mwaona, inu mwaona pamene inu munamuweruza Iye. Iye ali pa mlandu kwa aliyense wa inu, Iye ali pano pamaso panu, Mawu Ake ali pano, Iye amatsimikizira Mawu Ake. Inu muli pano, Iye— Iye ali pa mlandu kwa inu, osati pa mlandu kwa ine, ine ndimamukhulupirira Iye, Iye ali pa mlandu kwa inu. Ndipo ngati inu mukumukhulupirira Iye, ndipo ngati inu mumuweruza Iye wokhulupirika ku Mawu Ake. . .

¹⁷⁰ Tsopano iwo ali pafupi kuwongola mzerewo, kotero iwo akupanga mozungulira, inu mwaona. Basi, ndikungodikirira mpaka iye atawongola iwo. Mungosunthira kunja ndi kupanga mzere wautali. Ndipo muzipita molunjika mmbuyo kumene inu munachokera, pamene inu muzituluka.

¹⁷¹ Ngati inu munamukhulupirira Iye, ndiye chinachake chichitika. Kumbukirani, tsopano, mulibe mphamvu mwa aliyense wa atomiki awa. Mulibe mphamvu mwa ine. Mulibe mphamvu mwa munthu aliyense, yochiritsa. Koma tiri ndi ulamuliro wochokera kwa Mulungu, wochitira izi. Ife tiribe mphamvu; ife tiri ndi ulamuliro. *Apa* pali ulamuliro wathu, Mawu a Mulungu, ndipo Kukhalapo kwa Yesu Khristu kukutsimikizira kuti Iye ali pano. Chiyani? Inu mukuyenera kuchiritsidwa, aliyense!

¹⁷² Tsopano tiyeni tonse tiweramitse mitu yathu pamene ife tikupereka pemphero limodzi. Ndipo M'bale Borders ayima apa, akutsogolera nyimbo ndi kuwalondolera anthu. Pamene inu muzidutsa tsopano, zipempherani ndi kumakhulupirira.

¹⁷³ Nonse amene mwasonkhana, abale otumikira. Inu mukuwona chifukwa chimene ine ndachitira izi. Kutu, pamene ndizichoka, osonkhana anu akhale akudziwa, nawonso, anthu awa amene achiritsidwe, inu ndi wantchito wa Mulungu, nanunso. Si mmodzi yekha ayi. Mulungu samangokhala ndi wantchito mmodzi; Iye ali nawo masauzande a iwo, onse amene angakhulupirire Iwo. Tiyeni tiweramitse mitu yathu. Inu muli ndi ufulu wokwanira basi kuti muzipempherera odwala, monga ine, Roberts, kapena wina aliyenseyo.

¹⁷⁴ Atate Akumwamba, ndikukuthokozaninso Inu, mu mtima mwanga, ndipo ndikudziwa mitima pano, Inu ndi olungamitsidwa kuti muyike izi mu Mawu, pakuti taziwona izo zikugwira ntchito, ndipo tikudziwa kuti ndi choonadi. Ndipo tikudziwa kuti izo zigwira ntchito kwa munthu aliyense. Ndipo ife tikupemphera kwa Inu tsopano, Ambuye, tikukonza moyo wathu womwe, pamene ife tikudziwa kuti Inu muli pano. Inu mwayankha. Inu munayankhula Mawu Anu kwa ife. Inu muli pano.

¹⁷⁵ Tsopano Inu mutidzozze ife, Ambuye, kuti pamene ife tikuyika manja athu pa anthu odwala awa, anthu odwala osauka akhala pano mu mvula iyi madzulo ano, mulole aliyense wa iwo achire, ndi kupita kwawo ndi kukakhala bwino. Mulole iwo akhale monga Abrahamu, “kuzitcha zinthu zimenezo zimene kunalibe, ngati kuti zinalipo,” chifukwa Mulungu anapanga lonjezo. Ndipo Inu munali Mmodzi amene munati, “Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachiritsidwa.” Inu simunanene konse kuti iwo adzachira nthawi yomweyo, koma Inu munati iwo akanadzachita izo. Ndipo ife tikukhulupirira izo, Ambuye. Mumuthandize aliyense—aliyense kuti akhulupirire

izo, Ambuye, pamene ife tikupereka msonkhanowu mdzanja Lanu. Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikutsatira Malamulo Anu. Amen.

¹⁷⁶ Tsopano mulole mzere wa pemphero uyambike. M'bale Borders, tengani malo. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]...mukukhulupirira? Ambuye akudalitseni inu.

¹⁷⁷ Chifukwa chimene ine ndinayika manja anga limodzi ndi inu abale otumikira, icho chinali chifukwa chakuti ena a inu nonse mumavutika, nanunso, inu mukudziwa, ndipo mwadzaziyika nokha kuno, kudzapempherera ena, kuteroko; izo sizabwino. Ine ndikukhulupirira, pamene ife tinagwirana manja athu pamodzi, ine ndikukhulupirira kuti Mulungu analemekeza chimenecho.

¹⁷⁸ Ndipo apa, tsopano, apa—apa pali iwo amene sanathe kufika ku msonkhano; tsopano tiyeni tipempherere, mipango iyi.

¹⁷⁹ Atate Akumwamba, ife timaphunzitsidwa mu Baibulo, kuti—kuti, “Iwo anatenga kuchokera ku thupi la Paulo Woyera, mipango ndi zovala.” Ife si Paulo Woyera, koma Inu mukadali Yesu. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mutumize madalitso Anu ndi mipango iyi, ndi kuchiza aliyense wa iwo. Achizeni iwo, Ambuye, kwa ulemelero Wanu. Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikupemphera ndi kuyitumiza iyo. Amen.

¹⁸⁰ Ine ndikufuna kuti ndinene ichi. Kuti, ndikubwera kudutsa mu mzere, ine ndimawona akazi ndi mwamuna atanyamula makanda, ndipo iwo anali atanyowa. Inu mudzangondikumbukira ine, abale anga azibusa, kuti, masabata kuchokera pano, inu mudzapeza kuti, panali chinthu chachikulu chimene chinachitika pano. Iwo achira. Ine ndikuti nainte peresenti a iwo achira. Uko nkulondola. Oh, ine izo zinali... Ine sindinamvererepo chikhulupiriro cha mtundu woterowo. Izo zinali zodabwitsa kwambiri. Ine ndikuwona inu... Tsopano mungochita, pitirirani ndi kukachita ngati zonse zatha, ziribe kanthu ngati inu simunamverere izo. Musatero... Iye sananene kuti, “Kodi inu munamverera izo?” Iye anati, “Kodi inu munakhulupirira izo? Kodi mukukhulupirira izo?” Ndipo ife tikukhulupirira izo. Ndipo Iye ali pano tsopano, ndipo ife tikumupatsa Iye—ifetse tikumupatsa Iye matamando ndi ulemelero, pa zonse zimene Iye wachita.

¹⁸¹ Ndipo abwenzi Achikhristu okondedwa, ine ndikudziwa kuti iwo akhala akutseka msonkhanowu mu maminiti pang'ono, ndipo ine ndikufuna kunena ichi kwa inu. Ngati ine sindidzakomana nanunso mbali iyi ya Mtsinje, ine ndidzakakuwonani inu Kumeneke ndi Uthenga womwewu, Chinthu chomwechi. Tsopano mungokumbukira, kuti chimene inu mwachivomereza masana ano, malingaliro anu akhala wogamula wanu. Icho chapanga malingaliro ake, chapanga chigamulo.

¹⁸² Tsopano inu mungopitiriza kumachita, ine sindikusamala ngati inu munafa ziwalo ndipo simumatha kusuntha, mungopitirira kukhulupirirabe izo, Iye—Iye anati, “Iwo adzachira! Iwo adzachira!” Izo ndi zomwe mboniyo inanena, mboni iliyonse lero. Njira yonse kudutsa mu Baibulo, Iye... pokhapokha Iye atanena chinachake chikanadzachitika mwachokha. Koma mu nkhani iyi, “Iwo adzachira,” ndiko kusanjika kwa manja. Tsopano ngati masomphenya anachitika, ndi kuti, “ichi chidzachitika pa nthawi inayake, nthawi inayake,” kenako Iye amayika nthawiyo. Koma pa nkhani iyi, Iye anati, “Iwo adzachira.” Mukhulupirire izo, ndi mtima wanu wonse. Tiyeni tiyimbe nthawi imodzi.

Mpaka tidzakomanenso! mpaka
tidzakomanenso!
Mpaka tidzakomanenso pa mapazi a Yesu;
Oh, mpaka tidzakomanenso! mpaka
tidzakomanenso!
Mulungu akhale nanu mpaka
tidzakomanenso!

¹⁸³ Tsopano basi tisanati, tiyeni tigwirane chanza ndi winawake pafupi nanu, ndikuti, “Mulungu akudalitse iwe, mzanga Wachikhristu.” Musasunthe. Mungokhala, gwiranani chanza mozungulira. “Mulungu akudalitse iwe, mzanga Wachikhristu.” Mulungu akudalitse iwe. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitse iwe, Roy.

¹⁸⁴ Tsopano tiyeni tikweze manja athu kwa Khristu, ndipo tiyimbe.

Mpaka tidzakomanenso!
Tiyeni titseke maso athu ndi kukweza manja athu tsopano.
...mpaka tidzakomanenso!
Mpaka tidzakomanenso pa mapazi a Yesu! 

64-0405 Mlandu
4-H Club Barn
Louisville, Mississippi U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org